

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

KUKONDA MULUNGU

**Tingaonetse bwanji chikondi
chathu kwa Mulungu?**

*“Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu,
kuti tisunge Malamulo ache: ndipo
malamulo ache sali olemetsa.”*
(1 Yohane 5v3)

Written by:
Mick Alexander
Email: leandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

KUKONDA MULUNGU

**Tingaonetse bwanji chikondi
chathu kwa Mulungu?**

*“Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu,
kuti tisunge Malamulo ache: ndipo
malamulo ache sali olemetsa.”*
(1 Yohane 5v3)

Written by:
Mick Alexander
Email: leandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Agalatiya 5v6 akuti: “...komatu chikhulupiliro chakuchititsa mwa chikondi.” Choncho m’ malo mosunga uchimo, tiyeni tikhululukirane wina ndi mzake ndi kutsatira **1 Petro 4v8** yemwe akuti: “..mukhale nacho chikondano chenicheni mwa inu nokha, pakuti chikondano chikwiriritsa unyinjira wa machimo.”

Pomaliza **1 Akorinto 13v4-8** akuti,
“Chikondi chikhala chilezere,
chiri chokoma mtima.
Chikondi sichidukidwa;
chikondi sichidziwa kudzitamanda,
Sichidzikuza, sichichita zosayenera,
sichitsata za mwini yekha,
Sichipsa mtima, sichilingilira zoipa.
Sichikondwera ndi chinyengo,
koma chikondwera ndi choonadi.
Chikwilira zinthu zonse,
chikhulupilira zinthu zonse,
chiyembekeza zinthu zonse,
chipilira zinthu zonse.

Chikondi sichilephera”.

Ambuye akudalitseni pamene mukupitiliza kuyenda naye.

Agalatiya 5v6 akuti: “...komatu chikhulupiliro chakuchititsa mwa chikondi.” Choncho m’ malo mosunga uchimo, tiyeni tikhululukirane wina ndi mzake ndi kutsatira **1 Petro 4v8** yemwe akuti: “..mukhale nacho chikondano chenicheni mwa inu nokha, pakuti chikondano chikwiriritsa unyinjira wa machimo.”

Pomaliza **1 Akorinto 13v4-8** akuti,
“Chikondi chikhala chilezere,
chiri chokoma mtima.
Chikondi sichidukidwa;
chikondi sichidziwa kudzitamanda,
Sichidzikuza, sichichita zosayenera,
sichitsata za mwini yekha,
Sichipsa mtima, sichilingilira zoipa.
Sichikondwera ndi chinyengo,
koma chikondwera ndi choonadi.
Chikwilira zinthu zonse,
chikhulupilira zinthu zonse,
chiyembekeza zinthu zonse,
chipilira zinthu zonse.

Chikondi sichilephera”.

Ambuye akudalitseni pamene mukupitiliza kuyenda naye.

kwa anthu otizungulira. Pamene tikumana ndi munthu pa njira, tizifunse tokha kuti; ‘kodi munthu uyu akupita kumwamba kapena ku Gehena?’ Mwina sizingatheke kuchitira umboni munthu wina aliyense, koma pamene Mulungu atipatsa mpata, tikuyenera kuchitira umboni za Yesu.

POMALIZA

Mulungu akutiya pa **1 Samueli 2v30** kuti: “..popeza amene andilemekeza Inenso ndidzawalemekeza...” Njira yopelekera ulemu kwa Mulungu ndikupereka njira zathu kwa Iye komanso kukhala ndi chikhulupiliro pa Iye monga chikhulupiliro cha mwana pa atate wake. Tikuzidwa pa **Aheberi 11v6** kuti: “koma wopanda chikhulupiliro sikutheka kumkondweretsa, pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupilira kuti alipo, ndi kuti ali wobwenzera mphotho iwo akumfuna Iye.” Tonse tikudziwa kuti Mulungu samanama, choncho pamene tikulemekeza Mulungu; (pokhulupilira zomwe zalembedwa komanso kuyenda mu chikhulupiliro) Mulungu adzatilipira munjira yakuti tidzadziwa kuti Mulungu akulemekeza chikhulupiliro chathu mwa Iye.

kwa anthu otizungulira. Pamene tikumana ndi munthu pa njira, tizifunse tokha kuti; ‘kodi munthu uyu akupita kumwamba kapena ku Gehena?’ Mwina sizingatheke kuchitira umboni munthu wina aliyense, koma pamene Mulungu atipatsa mpata, tikuyenera kuchitira umboni za Yesu.

POMALIZA

Mulungu akutiya pa **1 Samueli 2v30** kuti: “..popeza amene andilemekeza Inenso ndidzawalemekeza...” Njira yopelekera ulemu kwa Mulungu ndikupereka njira zathu kwa Iye komanso kukhala ndi chikhulupiliro pa Iye monga chikhulupiliro cha mwana pa atate wake. Tikuzidwa pa **Aheberi 11v6** kuti: “koma wopanda chikhulupiliro sikutheka kumkondweretsa, pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupilira kuti alipo, ndi kuti ali wobwenzera mphotho iwo akumfuna Iye.” Tonse tikudziwa kuti Mulungu samanama, choncho pamene tikulemekeza Mulungu; (pokhulupilira zomwe zalembedwa komanso kuyenda mu chikhulupiliro) Mulungu adzatilipira munjira yakuti tidzadziwa kuti Mulungu akulemekeza chikhulupiliro chathu mwa Iye.

KUKONDA MULUNGU

Tingaonetse bwanji chikondi chathu kwa Mulungu?

“Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge Malamulo ache: ndipo malamulo ache sali olemetsa.”

(1 Yohane 5v3)

CHIKONDI CHA MULUNGU PA IFE

Chikondi cha Mulungu pa ife ndi chachikulu ndipo Yesu anaonetsera chikondi chake pa ife pamene anafa pa mtanda m’ malo mwa inu ndi ine. **Aroma 5v8** akuti: “koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m’menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife.” Komanso **Yohane 3v16** akuti: “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake obadwa yekha kuti yense wakukhulupilira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.” Pali mavesi ochuluka omwe akunena za chikondi cha Mulungu komanso m’mene Iye anaonetsera chikondi chake kudzera mwa Yesu Khristu kuti

KUKONDA MULUNGU

Tingaonetse bwanji chikondi chathu kwa Mulungu?

“Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu, kuti tisunge Malamulo ache: ndipo malamulo ache sali olemetsa.”

(1 Yohane 5v3)

CHIKONDI CHA MULUNGU PA IFE

Chikondi cha Mulungu pa ife ndi chachikulu ndipo Yesu anaonetsera chikondi chake pa ife pamene anafa pa mtanda m’ malo mwa inu ndi ine. **Aroma 5v8** akuti: “koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m’menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife.” Komanso **Yohane 3v16** akuti: “Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake obadwa yekha kuti yense wakukhulupilira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.” Pali mavesi ochuluka omwe akunena za chikondi cha Mulungu komanso m’mene Iye anaonetsera chikondi chake kudzera mwa Yesu Khristu kuti

tsopano, wina aliyense amene alapa machimo, nakhulupilira mwa Yesu, amabadwa mwatsopano ndikukhala mwana wa Mulungu. Ndizodabwitsa kudziwa kuti Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi anabwera panso pano kuchokera kumwamba, kudzakhala pakati pathu, ndikutifera kuti tikakhululukidwe ndikukhala ana a Mulungu. **1 Yohane 3v1** akuti: “*Taonani chikondicho cha Mulungu pa ife ndi chachikulu.*” Ndipo pokhala ife tsopano ana ake, tingamuonetse bwanji Atate wathu wa kumwamba chikondi chomuyenera?

TINGAMUONETSE BWANJI MULUNGU KUTI TIMAMUKONDA?

Pa **Yohane 14v23** Yesu akuti: “*Ngati wina akonda Ine, adzasunga mawu anga...*” Choncho tikuona kuti tingamuonetse Mulungu chikondi chathu pamene timvera malamulo ake. **1 Yohane 5v3** akukamba chimodzimodzi pamene akutiwiza kuti kumvera Mulungu sikolemetsa. Akuti: “*Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu kuti tisunge malamulo ake, ndipo malamulo ake sali olemetsa.*” Mulungu sakutifunsa kuchita chinthu chosatheka, koma kudzera mwa Mzimu Woyera, Mulungu amatipatsa mphamvu yomvera. Mzimu

tsopano, wina aliyense amene alapa machimo, nakhulupilira mwa Yesu, amabadwa mwatsopano ndikukhala mwana wa Mulungu. Ndizodabwitsa kudziwa kuti Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi anabwera panso pano kuchokera kumwamba, kudzakhala pakati pathu, ndikutifera kuti tikakhululukidwe ndikukhala ana a Mulungu. **1 Yohane 3v1** akuti: “*Taonani chikondicho cha Mulungu pa ife ndi chachikulu.*” Ndipo pokhala ife tsopano ana ake, tingamuonetse bwanji Atate wathu wa kumwamba chikondi chomuyenera?

TINGAMUONETSE BWANJI MULUNGU KUTI TIMAMUKONDA?

Pa **Yohane 14v23** Yesu akuti: “*Ngati wina akonda Ine, adzasunga mawu anga...*” Choncho tikuona kuti tingamuonetse Mulungu chikondi chathu pamene timvera malamulo ake. **1 Yohane 5v3** akukamba chimodzimodzi pamene akutiwiza kuti kumvera Mulungu sikolemetsa. Akuti: “*Pakuti ichi ndi chikondi cha Mulungu kuti tisunge malamulo ake, ndipo malamulo ake sali olemetsa.*” Mulungu sakutifunsa kuchita chinthu chosatheka, koma kudzera mwa Mzimu Woyera, Mulungu amatipatsa mphamvu yomvera. Mzimu

Ngati tikudziwa m’bale kapena mlongo amene sakuyenda bwino ndi Ambuye, tikuyenera kulankhula nawo ndikuwauza kuti alape. **Agalatiya 6v1** akuti: “*Abale, ngatinso munthu agwidwa nako kulakwa kwakuti, inu auzimu mubwenze otereyo mu mzimu wa chifatso*” Ndikofunika kuwabwenza kukulapa chifukwa chipulumutso chawo chifunikira kuti ayende moyo wa chiyeero. Izi zikhoza kukhala zovuta kuchita popeza m’baleyo akhoza osakondwa, kapena kuchita manyazi, mwina osamvetsa kumene, choncho tikuyenera kumufikira modekha. **Yakobo 5v19-20** akuti: “*Abale anga, ngati wina wa inu asochera posiyana ndi choonadi, ndipo ambwenza iye mzache; azindikire, kuti iye amene abwenza ochimwa kunjira yache yosochera, adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvundikira machimo aunyinji.*” Mavesiwa akutifotokozera kufunika kolankhula ndi m’bale kapena mlongo amene akupita kuchitayiko. Tikuyenera kuwapulumutsa ku mkwiyo woopsa wa Mulungu.

Palibe chinthu chofunikira choposa chipulumutso. Nthawi ina ili yonse yomwe tingakhale ndi mpata, tichitire umboni za Yesu

Ngati tikudziwa m’bale kapena mlongo amene sakuyenda bwino ndi Ambuye, tikuyenera kulankhula nawo ndikuwauza kuti alape. **Agalatiya 6v1** akuti: “*Abale, ngatinso munthu agwidwa nako kulakwa kwakuti, inu auzimu mubwenze otereyo mu mzimu wa chifatso*” Ndikofunika kuwabwenza kukulapa chifukwa chipulumutso chawo chifunikira kuti ayende moyo wa chiyeero. Izi zikhoza kukhala zovuta kuchita popeza m’baleyo akhoza osakondwa, kapena kuchita manyazi, mwina osamvetsa kumene, choncho tikuyenera kumufikira modekha. **Yakobo 5v19-20** akuti: “*Abale anga, ngati wina wa inu asochera posiyana ndi choonadi, ndipo ambwenza iye mzache; azindikire, kuti iye amene abwenza ochimwa kunjira yache yosochera, adzapulumutsa munthu kwa imfa, ndipo adzabvundikira machimo aunyinji.*” Mavesiwa akutifotokozera kufunika kolankhula ndi m’bale kapena mlongo amene akupita kuchitayiko. Tikuyenera kuwapulumutsa ku mkwiyo woopsa wa Mulungu.

Palibe chinthu chofunikira choposa chipulumutso. Nthawi ina ili yonse yomwe tingakhale ndi mpata, tichitire umboni za Yesu

tikuyenera kufalitsa Uthenga wabwino wa Yesu pamene tili ndi mpata.

Pali njira zambiri zomwe tingawauzire anthu za Yesu:

- 1) Auzeni za chiyembekezo chanu cha kumwamba.
- 2) Auzeni m'mene Mulungu wasinthira moyo wanu ndi kukupulumutsani ku moyo wa uchimo.
- 3) Pelekani timabuku tolemba za Uthenga kwa anthu omwe mukumana nawo.
- 4) Ikani timabuku tolemba za Uthenga ku ma bokosi a anthu ku Positi Ofesi.
- 5) Ayitanireni anthu ku tchalitchi.
- 6) Apatseni baibulo kapena CD yokamba za Uthenga wa Yesu.
- 7) Lalikirani mu nseu.
- 8) Lembani makalata kapena kuyimba ma telefoni.

Tikuyenera, kudzera mu pemphero, kumufunsa Mulungu kuti atitsogolere kwa anthu oti tiwauze za Uthenga, komanso kuti atipatse mawu oti tikalankhule monga **1 Petro 3v15** akunenera: "... komatu ndi chifatso ndi mantha."

tikuyenera kufalitsa Uthenga wabwino wa Yesu pamene tili ndi mpata.

Pali njira zambiri zomwe tingawauzire anthu za Yesu:

- 1) Auzeni za chiyembekezo chanu cha kumwamba.
- 2) Auzeni m'mene Mulungu wasinthira moyo wanu ndi kukupulumutsani ku moyo wa uchimo.
- 3) Pelekani timabuku tolemba za Uthenga kwa anthu omwe mukumana nawo.
- 4) Ikani timabuku tolemba za Uthenga ku ma bokosi a anthu ku Positi Ofesi.
- 5) Ayitanireni anthu ku tchalitchi.
- 6) Apatseni baibulo kapena CD yokamba za Uthenga wa Yesu.
- 7) Lalikirani mu nseu.
- 8) Lembani makalata kapena kuyimba ma telefoni.

Tikuyenera, kudzera mu pemphero, kumufunsa Mulungu kuti atitsogolere kwa anthu oti tiwauze za Uthenga, komanso kuti atipatse mawu oti tikalankhule monga **1 Petro 3v15** akunenera: "... komatu ndi chifatso ndi mantha."

Woyera amakhala mwa okhulupilira, kuwapatsa mphamvu yakutsatira malamulo a Mulungu. Choncho, tiyeni tione malamulo amenewa.

Pa **Mateyu 22v36-40** Yesu anafunsidwa kuti lamulo loposa onse ndi liti, ndipo iye anati: "*Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako onse, ndi moyo wako onse ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndi ili, uzikonda mzako monga udzikonda iwe mwini. Pamalamulo awa awiri, mpokolowekapo chilamulo chonse cha aneneri.*" Tikhoza kuona kuti malamulo onse a Mulungu akumangilidwa mu malamulo awiri ndipo ndi awa:

1) Kukonda Mulungu

2) Kukonda mzako

Tikayang'ana mwachidule malamulo khumi, pa **Deutoronomo 5v6-22**, tiona kuti oyamba anayi akukamba zakukonda Mulungu ndipo asanu ndi limodzi akukamba za kukondana wina ndi mzake. Tiyeni tiwaone malamulo amenewa mwachidule.

Woyera amakhala mwa okhulupilira, kuwapatsa mphamvu yakutsatira malamulo a Mulungu. Choncho, tiyeni tione malamulo amenewa.

Pa **Mateyu 22v36-40** Yesu anafunsidwa kuti lamulo loposa onse ndi liti, ndipo iye anati: "*Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako onse, ndi moyo wako onse ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndi ili, uzikonda mzako monga udzikonda iwe mwini. Pamalamulo awa awiri, mpokolowekapo chilamulo chonse cha aneneri.*" Tikhoza kuona kuti malamulo onse a Mulungu akumangilidwa mu malamulo awiri ndipo ndi awa:

1) Kukonda Mulungu

2) Kukonda mzako

Tikayang'ana mwachidule malamulo khumi, pa **Deutoronomo 5v6-22**, tiona kuti oyamba anayi akukamba zakukonda Mulungu ndipo asanu ndi limodzi akukamba za kukondana wina ndi mzake. Tiyeni tiwaone malamulo amenewa mwachidule.

MALAMULO KHUMI

Malamulo anayi oyamba akukamba za ubale wathu ndi Mulungu. Akutifotokozerana:

1) Tisakhale ndi Mulungu wina chifukwa pali Mulungu m' modzi yekha ndipo milungu yina ndi mafano kapena kuti ziwanda.

2) Tisazipangire fano kapena chifaniziro chiri chonse cha zinthu kapena munthu. Pasakhale kanthu kena pakati pa ife ndi Mulungu ndipo izi zikhonza kukhala chuma, masewera, ntchito kapena banja. Tikhalenso osamala, osalola chuma kapena zinthu zathu kukhala milungu kapena mafano kwa ife. Mulungu asakhale wachiwiri m' moyo mwathu.

3) Tisatchule dzina la Mulungu wathu pachabe. Tisanyoze dzina la Mulungu wathu. Timanyoza dzina la Mulungu pamene tinena kuti ndife akhristu koma tikunena ndi kuchita zinthu zonyoza komanso zotsutsana ndi Mulungu.

4) Tipatule tsiku limodzi pa sabata. Tikuuzidwa pa **Eksodo 23v12** kuti: *“Uzichita ntchito yako masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku la chisanu ndi chiwiri uzipumula, kuti ng'ombe yako ndi bulu wako zipumule ndi kuti mwana wa m' dzakazi wako ndi mlendo atsitsimuke.”* Ndipo

MALAMULO KHUMI

Malamulo anayi oyamba akukamba za ubale wathu ndi Mulungu. Akutifotokozerana:

1) Tisakhale ndi Mulungu wina chifukwa pali Mulungu m' modzi yekha ndipo milungu yina ndi mafano kapena kuti ziwanda.

2) Tisazipangire fano kapena chifaniziro chiri chonse cha zinthu kapena munthu. Pasakhale kanthu kena pakati pa ife ndi Mulungu ndipo izi zikhonza kukhala chuma, masewera, ntchito kapena banja. Tikhalenso osamala, osalola chuma kapena zinthu zathu kukhala milungu kapena mafano kwa ife. Mulungu asakhale wachiwiri m' moyo mwathu.

3) Tisatchule dzina la Mulungu wathu pachabe. Tisanyoze dzina la Mulungu wathu. Timanyoza dzina la Mulungu pamene tinena kuti ndife akhristu koma tikunena ndi kuchita zinthu zonyoza komanso zotsutsana ndi Mulungu.

4) Tipatule tsiku limodzi pa sabata. Tikuuzidwa pa **Eksodo 23v12** kuti: *“Uzichita ntchito yako masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku la chisanu ndi chiwiri uzipumula, kuti ng'ombe yako ndi bulu wako zipumule ndi kuti mwana wa m' dzakazi wako ndi mlendo atsitsimuke.”* Ndipo

ndipo Yesu anapereka lamulo latsopano. Pa **Yohane 13v34-35** akuti: *“Ndikupatsani inu lamulo latsopano kuti mukondane wina ndi mzake; monga ndakonda inu kuti inunso mukondane wina ndi mzake. Mwa ichi, adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondi wina ndi mzake.”* Tikuyenera kukhala ndi mtendere ndi anthu onse ndipo anthu osakhulupilira akaona ife tikutero, osadana monga dziko lichitira, udzakhala umboni ku chikhulupiliro chatu ndipo tidzaitanira anthu ochuluka kwa Yesu Khristu.

KUCHITIRA UMBONI ZA YESU

Mfundo yomaliza yomwe ndifuna kugawana nanu ndiyakuti tikuyenera kufalitsa uthenga wabwino komanso kuchitira umboni zomwe Yesu anatichitira ife. Pa **Marko 16v15-16** Yesu anauza ophunzira ake kuti: *“Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupilira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupilira adzalangidwa.”* Munthu wina aliyense amene ali pa dziko lapansi akupita kumwamba kapena ku Gehena, choncho

ndipo Yesu anapereka lamulo latsopano. Pa **Yohane 13v34-35** akuti: *“Ndikupatsani inu lamulo latsopano kuti mukondane wina ndi mzake; monga ndakonda inu kuti inunso mukondane wina ndi mzake. Mwa ichi, adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondi wina ndi mzake.”* Tikuyenera kukhala ndi mtendere ndi anthu onse ndipo anthu osakhulupilira akaona ife tikutero, osadana monga dziko lichitira, udzakhala umboni ku chikhulupiliro chatu ndipo tidzaitanira anthu ochuluka kwa Yesu Khristu.

KUCHITIRA UMBONI ZA YESU

Mfundo yomaliza yomwe ndifuna kugawana nanu ndiyakuti tikuyenera kufalitsa uthenga wabwino komanso kuchitira umboni zomwe Yesu anatichitira ife. Pa **Marko 16v15-16** Yesu anauza ophunzira ake kuti: *“Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupilira nabatizidwa, adzapulumutsidwa; koma amene sakhulupilira adzalangidwa.”* Munthu wina aliyense amene ali pa dziko lapansi akupita kumwamba kapena ku Gehena, choncho

akamasuke ndi inu musautsidwe.” Mulungu sakuyembekezera ife kupereka moposera kupeza kwathu, koma pamene tiri nazo zochuluka, tiri afulu kupereka mochuluka, moolowa manja komanso mwa nsangala.

Chinthu china chofunika kwambiri ndi chakuti tikuyenera kukhululukira iwo akutichimwira, angakhale adani athu. (**Mateyu 5v43-48**) Mulungu anakhululukira inu ndi ine ku uchimo ndipo akulamulira ife kukhululukira anzathu. Kukhululukira kuli ndi mphamvu yochotsa udani ndikuyikapo chikondi. Yesu akutichenjeza mwakuya pokhudza kukana kukhululukira mzako. Pa **Mateyu 6v14-15** akuti: *“Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zao adzakhululukira inunso Atate wanu wa kumwamba. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zao, Atate wanunso sadzakhululukira zolakwa zanu.”* Ndikofunikira kukhululukira nthawi zonse, chifukwa ngati sititero, Mulungu sadzatikhululukira ndipo tidzakathera ku Gehena. Kukhululukira ndi stepe yoyamba ya ubale wa chikondi ndi mzathu yemwe takhala tisakukondana naye. Kukhululukira ndi kukondana wina ndi mzake ndizofunikira koposa

akamasuke ndi inu musautsidwe.” Mulungu sakuyembekezera ife kupereka moposera kupeza kwathu, koma pamene tiri nazo zochuluka, tiri afulu kupereka mochuluka, moolowa manja komanso mwa nsangala.

Chinthu china chofunika kwambiri ndi chakuti tikuyenera kukhululukira iwo akutichimwira, angakhale adani athu. (**Mateyu 5v43-48**) Mulungu anakhululukira inu ndi ine ku uchimo ndipo akulamulira ife kukhululukira anzathu. Kukhululukira kuli ndi mphamvu yochotsa udani ndikuyikapo chikondi. Yesu akutichenjeza mwakuya pokhudza kukana kukhululukira mzako. Pa **Mateyu 6v14-15** akuti: *“Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zao adzakhululukira inunso Atate wanu wa kumwamba. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zao, Atate wanunso sadzakhululukira zolakwa zanu.”* Ndikofunikira kukhululukira nthawi zonse, chifukwa ngati sititero, Mulungu sadzatikhululukira ndipo tidzakathera ku Gehena. Kukhululukira ndi stepe yoyamba ya ubale wa chikondi ndi mzathu yemwe takhala tisakukondana naye. Kukhululukira ndi kukondana wina ndi mzake ndizofunikira koposa

Levitiko 23v3 akuti: *“...koma lachisanu ndi chiwiri ndilo sabata lakupumula, msonkhano wopatulika.”* Ngati tigwira ntchito tsiku liri lonse pa sabata, ntchito idzakhala fano kwa ife ndipo sitidzakhala ndi nthawi yakumupembedza Mulungu, kapena kukhala ndi nthawi ndi mabanja athu. Zokhudza sabata, tikuuzidwa pa **Aroma 14v5-6** kuti m’khristu aliyense ali waufulu kusankha tsiku pa sabata lomwe liri lopatulika kwa iye, ndipo ine pandekha ndikukhulupilira kuti tsiku liri lonse liri lopatulika pamaso pa Mulungu. Ndichinyengo kukhala woyera tsiku limodzi pa sabata ndikukhala osapembedza masiku ena asanu ndi limodzi. Tiyeni tikhale woyera tsiku ndi tsiku.

Malamulo asanu ndi limodzi otsirizawa akukamba za ubale wathu ndi anzathu. Malamulowa akuti:

- 1) Tilemekeze atate wathu ndi amayi wathu
- 2) Tisaphe
- 3) Tisachite chigololo
- 4) Tisabe
- 5) Tisaname
- 6) Tisasilire. Kusilira ndikufuna zinthu zomwe sizathu kuti zikhale zathu.

Levitiko 23v3 akuti: *“...koma lachisanu ndi chiwiri ndilo sabata lakupumula, msonkhano wopatulika.”* Ngati tigwira ntchito tsiku liri lonse pa sabata, ntchito idzakhala fano kwa ife ndipo sitidzakhala ndi nthawi yakumupembedza Mulungu, kapena kukhala ndi nthawi ndi mabanja athu. Zokhudza sabata, tikuuzidwa pa **Aroma 14v5-6** kuti m’khristu aliyense ali waufulu kusankha tsiku pa sabata lomwe liri lopatulika kwa iye, ndipo ine pandekha ndikukhulupilira kuti tsiku liri lonse liri lopatulika pamaso pa Mulungu. Ndichinyengo kukhala woyera tsiku limodzi pa sabata ndikukhala osapembedza masiku ena asanu ndi limodzi. Tiyeni tikhale woyera tsiku ndi tsiku.

Malamulo asanu ndi limodzi otsirizawa akukamba za ubale wathu ndi anzathu. Malamulowa akuti:

- 1) Tilemekeze atate wathu ndi amayi wathu
- 2) Tisaphe
- 3) Tisachite chigololo
- 4) Tisabe
- 5) Tisaname
- 6) Tisasilire. Kusilira ndikufuna zinthu zomwe sizathu kuti zikhale zathu.

Pamene timvera malamulo amenewa, sitimuchimwira Mulungu kapena kulakwira m'bale wathu. Mulungu amadana ndi tchimo, choncho pamene timvera malamulo ake, tikulemekeza ulamuliro wake ndiponso kumuonetsera chikondi chathu. Wina aliyense amene amakonda Mulungu, amakondanso m'bale wake chifukwa chikondi cha Mulungu chimayenda mwa iye ndikusefukira mwa anthu ena. Komanso, aliyense okonda m'bale wake, akonda Mulungu chifukwa akumvera lamulo lake lokondana wina ndi mzake. Kukonda Mulungu ndi kukonda m'bale wako zimayendera limodzi. Tikuuzidwa pa **Aroma 13v8-10** kuti "*Musakhale ndi mangawa kwa munthu aliyense, koma kukondana ndiko, pakuti iye amene akondana ndi mzake wakwanitsa lamulo. Pakuti ili, usachite chigololo, usaphe, usabe, usasilire, ndipo lingakhale lamulo lina liri lonse, limangika pamodzi m'mawu amenewa, kuti, Uzikonda mzako monga udzikonda iwe mwini. Chikondano sichichitira mzake choipa; chotero chikondanocho chiri chokwaniritsa lamulo.*" Kuchokera ku mavesi awa, tikuona kuti chikondi chizikhala cholinga chathu nthawi zonse chifukwa chikondi chikwaniritsa lamulo. Pa

chao, ndikudzisungira mwini wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi." Ndipo **Yakobo 2v15-16** akuti: "*M'bale kapena mlongo akakhala wausiwa, nichikamsowa chakudya cha tsiku lake, ndipo wina wa inu akanena nawo, mukani ndi mtendere ndi kukhuta, osawapatsa iwo zosowa zapathupi; kupindula kwake nchiani?*" Kuchokera pa mavesi amenewa, tikuona kuti ngati tingathe, tikuyenera kuthandiza m'bale kapena mlongo amene ali osowa, osati kungomufunira zabwino ndikumusiya opanda kanthu.

Pamene tikupereka kuthandiza osowa tikuyenera kupereka ku mpingo kuti mpingo ukathe kuthandizira utumiki komanso atsogoleri ake. Izi zichitike ndi mtima wokondwera monga **2 Akorinto 9v7** akunenera: "*Yense achite monga atsimikiza mtima, si mwa chisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwera.*" Komanso Mulungu sakutipempha kupereka ndikukhala osauka ayi, koma kupereka m'mene tingathere. **2 Akorinto 8v12-13** akuti: "*Pakuti ngati chibvomerezo chiri pomwepo, munthu alandiridwa monga momwe ali nacho, si monga chimsowa. Pakuti sinditero kuti ena*

Pamene timvera malamulo amenewa, sitimuchimwira Mulungu kapena kulakwira m'bale wathu. Mulungu amadana ndi tchimo, choncho pamene timvera malamulo ake, tikulemekeza ulamuliro wake ndiponso kumuonetsera chikondi chathu. Wina aliyense amene amakonda Mulungu, amakondanso m'bale wake chifukwa chikondi cha Mulungu chimayenda mwa iye ndikusefukira mwa anthu ena. Komanso, aliyense okonda m'bale wake, akonda Mulungu chifukwa akumvera lamulo lake lokondana wina ndi mzake. Kukonda Mulungu ndi kukonda m'bale wako zimayendera limodzi. Tikuuzidwa pa **Aroma 13v8-10** kuti "*Musakhale ndi mangawa kwa munthu aliyense, koma kukondana ndiko, pakuti iye amene akondana ndi mzake wakwanitsa lamulo. Pakuti ili, usachite chigololo, usaphe, usabe, usasilire, ndipo lingakhale lamulo lina liri lonse, limangika pamodzi m'mawu amenewa, kuti, Uzikonda mzako monga udzikonda iwe mwini. Chikondano sichichitira mzake choipa; chotero chikondanocho chiri chokwaniritsa lamulo.*" Kuchokera ku mavesi awa, tikuona kuti chikondi chizikhala cholinga chathu nthawi zonse chifukwa chikondi chikwaniritsa lamulo. Pa

chao, ndikudzisungira mwini wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi." Ndipo **Yakobo 2v15-16** akuti: "*M'bale kapena mlongo akakhala wausiwa, nichikamsowa chakudya cha tsiku lake, ndipo wina wa inu akanena nawo, mukani ndi mtendere ndi kukhuta, osawapatsa iwo zosowa zapathupi; kupindula kwake nchiani?*" Kuchokera pa mavesi amenewa, tikuona kuti ngati tingathe, tikuyenera kuthandiza m'bale kapena mlongo amene ali osowa, osati kungomufunira zabwino ndikumusiya opanda kanthu.

Pamene tikupereka kuthandiza osowa tikuyenera kupereka ku mpingo kuti mpingo ukathe kuthandizira utumiki komanso atsogoleri ake. Izi zichitike ndi mtima wokondwera monga **2 Akorinto 9v7** akunenera: "*Yense achite monga atsimikiza mtima, si mwa chisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwera.*" Komanso Mulungu sakutipempha kupereka ndikukhala osauka ayi, koma kupereka m'mene tingathere. **2 Akorinto 8v12-13** akuti: "*Pakuti ngati chibvomerezo chiri pomwepo, munthu alandiridwa monga momwe ali nacho, si monga chimsowa. Pakuti sinditero kuti ena*

akutiuzwa kuti mwamuna akuyenera kukhala mutu wa banja. Pa **Aefeso 5v22**, akazi akuuzidwa: “Akazi inu, mverani amuna anu a inu eni, monga kumvera Ambuye.” Izi sizitanthauza kuti mkazi akhale ngati kapolo kwa mwamuna ayi, koma alemekeze ulamuliro wake. Amuna akupatsidwa malangizo apadera kukonda akazi awo monga Khristu anakonda ife. **Aefeso 5v25** akuti: “Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Ekelesia, nadzipereka yekha m'malo mwake.” Ndipo **1 Petro 3v7** akuti: “Momwemonso amuna inu, khalani nawo monga mwa chidziwitso, ndikuchitira mkazi ulemu monga chotengera chochepe m'phamvu, monganso wolowa nyumba pamodzi wa chisomo cha moyo, kuti mapemphero anu angaletsedwe.” Kuchokera ku mavesi awa, tikuona kufunika komwe Mulungu amaika pakukonda akazi athu komanso ana athu. Banja lopanda mtendere lidzasokoneza mapemphero athu.

Mulungu akufunanso ife kuti tithandize iwo amene sangathe kuzithandiza okha. **Yakobo 1v27** akuti: “Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: kucheza ndi ana a masiye ndi akazi amasiye m'chisautso

akutiuzwa kuti mwamuna akuyenera kukhala mutu wa banja. Pa **Aefeso 5v22**, akazi akuuzidwa: “Akazi inu, mverani amuna anu a inu eni, monga kumvera Ambuye.” Izi sizitanthauza kuti mkazi akhale ngati kapolo kwa mwamuna ayi, koma alemekeze ulamuliro wake. Amuna akupatsidwa malangizo apadera kukonda akazi awo monga Khristu anakonda ife. **Aefeso 5v25** akuti: “Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Ekelesia, nadzipereka yekha m'malo mwake.” Ndipo **1 Petro 3v7** akuti: “Momwemonso amuna inu, khalani nawo monga mwa chidziwitso, ndikuchitira mkazi ulemu monga chotengera chochepe m'phamvu, monganso wolowa nyumba pamodzi wa chisomo cha moyo, kuti mapemphero anu angaletsedwe.” Kuchokera ku mavesi awa, tikuona kufunika komwe Mulungu amaika pakukonda akazi athu komanso ana athu. Banja lopanda mtendere lidzasokoneza mapemphero athu.

Mulungu akufunanso ife kuti tithandize iwo amene sangathe kuzithandiza okha. **Yakobo 1v27** akuti: “Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: kucheza ndi ana a masiye ndi akazi amasiye m'chisautso

1 Petro 1v22 Mulungu akutiuzwa kuti: “..mukondane kwenikweni kuchokera mu mtima.”

MOYO WA CHIKHRISTU

Tsopano tiyeni tiyang'anitsitse chomwe Mulungu amafuna kuchokera kwa inu ndi ine. Malamulo khumi ndi pongoyambira pa moyo wa chikhristu. Chipangano chatsopano chikufotokoza mwakuya zomwe Mulungu akuyembekezera kwa ife. Mwachitsanzo, lamulo limodzi mwa malamulo khumi likuti usaphe koma **Mateyu 5** Yesu akuti kukwiwira m'bale wako ndichimodzimidzi ndi kupha ndipo tidzaweruzidwa. Lamulo lina likuti tisachite chigololo koma Yesu akuti tikasilira tachita chigololo mu mtima mwathu. Tisamalire mitima yathu ndipo tisalole malingaliro oyipa monga udani, kusilira, nsanje ndi zina zotero kukhala mwa ife. **1 Samueli 16v7** akuti: “... pakuti Yehova saona monga aona munthu, pakuti munthu ayang'ana chooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana mu mtima.”

Choncho chifukwa Mulungu amayang'ana mumtima nthawi zonse, maganizo auchimo akafika mu moyo wathu, tikuyenera kulapa

1 Petro 1v22 Mulungu akutiuzwa kuti: “..mukondane kwenikweni kuchokera mu mtima.”

MOYO WA CHIKHRISTU

Tsopano tiyeni tiyang'anitsitse chomwe Mulungu amafuna kuchokera kwa inu ndi ine. Malamulo khumi ndi pongoyambira pa moyo wa chikhristu. Chipangano chatsopano chikufotokoza mwakuya zomwe Mulungu akuyembekezera kwa ife. Mwachitsanzo, lamulo limodzi mwa malamulo khumi likuti usaphe koma **Mateyu 5** Yesu akuti kukwiwira m'bale wako ndichimodzimidzi ndi kupha ndipo tidzaweruzidwa. Lamulo lina likuti tisachite chigololo koma Yesu akuti tikasilira tachita chigololo mu mtima mwathu. Tisamalire mitima yathu ndipo tisalole malingaliro oyipa monga udani, kusilira, nsanje ndi zina zotero kukhala mwa ife. **1 Samueli 16v7** akuti: “... pakuti Yehova saona monga aona munthu, pakuti munthu ayang'ana chooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana mu mtima.”

Choncho chifukwa Mulungu amayang'ana mumtima nthawi zonse, maganizo auchimo akafika mu moyo wathu, tikuyenera kulapa

msanga, ndikuitanira pa dzina la Mulungu kuti atiyeretse ndikutipatsa mtima woyera monga Davide akunenera pa **Masalimo 51v10** pamene akuti: “*Mundilengere mtima woyera Mulungu, mukonze mzimu wokhazikika m’kati mwanga.*” Davide anayitana Mulungu kuti ayeretse mtima wake ndikumupatsa mphamvu za uzimu kukana tchimo. Ifenso tikuyenera kutero pamene maganizo athu atinyenga. Pa **2 Akorinto 10v5** akuti: “*...ndikugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Khristu.*” Pamene tiyesedwa ndi malingaliro oyipa, tikhale achangu kulapa, chifukwa tikhonza kuchimwa monga mmene **Yakobo 1v14-15** akunenera: “*koma munthu aliyense ayesedwa pamene chilakolako chake cha iye mwini chimkokera, nichimyenga. Pamenepo, chilakolakocho chitayima, chibala uchimo ndipo uchimo utakula msinkhu ubala imfa.*” Pa mavesi amenewa tikuchenjzedwa kuyipa kozengeleza kuthana ndi mayesero amene angatifikitse kuuchimo. Choncho, musalole malingaliro amenewa kukhazikika mwa inu, muwakane mofulumira.

Pamene tachimwa, tikuyenera kupempha chikhululukiro cha tchimo limelelo. Sitikuyenera

msanga, ndikuitanira pa dzina la Mulungu kuti atiyeretse ndikutipatsa mtima woyera monga Davide akunenera pa **Masalimo 51v10** pamene akuti: “*Mundilengere mtima woyera Mulungu, mukonze mzimu wokhazikika m’kati mwanga.*” Davide anayitana Mulungu kuti ayeretse mtima wake ndikumupatsa mphamvu za uzimu kukana tchimo. Ifenso tikuyenera kutero pamene maganizo athu atinyenga. Pa **2 Akorinto 10v5** akuti: “*...ndikugonjetsa ganizo lonse ku kumvera kwa Khristu.*” Pamene tiyesedwa ndi malingaliro oyipa, tikhale achangu kulapa, chifukwa tikhonza kuchimwa monga mmene **Yakobo 1v14-15** akunenera: “*koma munthu aliyense ayesedwa pamene chilakolako chake cha iye mwini chimkokera, nichimyenga. Pamenepo, chilakolakocho chitayima, chibala uchimo ndipo uchimo utakula msinkhu ubala imfa.*” Pa mavesi amenewa tikuchenjzedwa kuyipa kozengeleza kuthana ndi mayesero amene angatifikitse kuuchimo. Choncho, musalole malingaliro amenewa kukhazikika mwa inu, muwakane mofulumira.

Pamene tachimwa, tikuyenera kupempha chikhululukiro cha tchimo limelelo. Sitikuyenera

kumpemphanso Mulungu kuti atipulumutse kachiwiri, chifukwa sitimataya chipulumutso chathu pamene tachimwa. Pamene tinapulumutsidwa, tinapulumutsidwa. Tikuyenera kulapa ku tchimo liri lonse tingakumane nalo mu moyo wathu. Tonse timachimwa nthawi ndi nthawi ndipo Mulungu ali wololera nthawi zonse kutikhululukira monga momwe akunenera pa **1 Yohane 1v9**: “*Ngati tivomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi wolungama iye kuti atikhululukire machimo athu ndi kulisambitsa, kutichotsera chosalungama chiri chonse.*” Choncho, tiyeni tilape pamene Mzimu Woyera atitsutsa. Tikhonza kutaya chipulumutso chathu tikamufulatira Mulungu ndikupitiliza kuchimwa m’ malo molapa.

Kukonda anthu apabanja pathu ndizofunika. Ndizosavuta kukhala wa chifundo kwa anthu omwe sitimakhala nawo koma Mulungu sasangalala pamene tikhala achifundo kwa anthu adera koma ankhaza kwa anthu apabanja pathu. Zokhudza ana, **Aefeso 6v4** akuti: “*Ndipo atate inu, musakwiyitse ana anu; komatu muwalere iwo m’maleredwe ndi chilangizo cha Ambuye.*” Zokhudza ukwati, mawu a Mulungu nthawi zonse

kumpemphanso Mulungu kuti atipulumutse kachiwiri, chifukwa sitimataya chipulumutso chathu pamene tachimwa. Pamene tinapulumutsidwa, tinapulumutsidwa. Tikuyenera kulapa ku tchimo liri lonse tingakumane nalo mu moyo wathu. Tonse timachimwa nthawi ndi nthawi ndipo Mulungu ali wololera nthawi zonse kutikhululukira monga momwe akunenera pa **1 Yohane 1v9**: “*Ngati tivomereza machimo athu ali wokhulupirika ndi wolungama iye kuti atikhululukire machimo athu ndi kulisambitsa, kutichotsera chosalungama chiri chonse.*” Choncho, tiyeni tilape pamene Mzimu Woyera atitsutsa. Tikhonza kutaya chipulumutso chathu tikamufulatira Mulungu ndikupitiliza kuchimwa m’ malo molapa.

Kukonda anthu apabanja pathu ndizofunika. Ndizosavuta kukhala wa chifundo kwa anthu omwe sitimakhala nawo koma Mulungu sasangalala pamene tikhala achifundo kwa anthu adera koma ankhaza kwa anthu apabanja pathu. Zokhudza ana, **Aefeso 6v4** akuti: “*Ndipo atate inu, musakwiyitse ana anu; komatu muwalere iwo m’maleredwe ndi chilangizo cha Ambuye.*” Zokhudza ukwati, mawu a Mulungu nthawi zonse